

“Langizo la Zachipembedzo pa Umoyo Wogonana ndi Kubereka ndi Ufulu “Wolengedwa mu Chifaniziro cha Mulungu”

Atsogoleri aChipembedzo Kumwera kwa Africa Akuthandizira Umoyo Wogonana ndi Kubereka ndi Ufulu kwa Onse

1. CHIYAMBI

Ife, ngati agulu lachipembedzo, timakhulupiria kuti sitingangwonerera pamene anthu athu alibe zidziwitso za umoyo ndi ufulu wa zogonana ndi uchembere (SRHR) mdera lathu womwe umapangitsa imfa zapobereka zokwana 10% ndi 13%,¹ ndipo chiwerengero chamimba zaatsikana chokwana 95% padziko lapansi,² ndiponso vuto la HIV³ loti munthu m'modzi mwa anthu asanu aliwonse azaka pakati pa 15 ndi 49 kuti azipezeka ndi kachirombo ka HIV. Gulu na Atsikana osati Mbete⁴ likuwerengera kuti “pamaiko 20 kumene kumachulukitsa maukwati aana, maiko 15 amachokera kuAfrica.”⁵ Kumwera kwa Sahara 39% yaatsikana amakwatiwa asanakwane zaka 18 ndipo 13% yaatsikana ena amakwatiwa asanakwane zaka 15.⁶ Akwatibwi achicheperewa amapezeka kwambiri m'midzi, pakati pa anthu osauka ndiponso osadziwa kuwerenga.⁷ M'madera onsewatu muli magulu azachipembedzo.

Ndi udindo wathu tonse amene agulu lachipembedzo kugwiritsa ntchito utsogoleri wathu kuphunzitsa ndi kulimbikitsa njira zopezera zidziwitso zamakono za SRHR. Tikuzindikira kuti mfundo za SRHR zikupezeka m'maiko 13 mwamaiko 15 akumwera kwa Africa a SADC, ndipo kuti mfundo zina ndi zachikale zoyenera kusinthidwa kuti zigwirizane ndi chikonzero cha SRHR ya SADC kuyambira chaka cha 2019 mpaka 2030.⁸

Ngati magulu achipembedzo kumwera kwa Africa, takhala tikupeza, ndipo tidzapitiliza kupeza mayankho, okhudzana ndi mavuto a SRHR. Takhala tikugwira ntchito mwakhama kupewetsa mimba zosakonzekera, komanso kupeza mayankho a vuto lamaukwati aana, nkhanza za amayi, ndi HIV / AIDS.⁹ Ngakhale tikuvomereza kuti “zotsatira zantchito yathu sizopambana zokhazoka, nthawi zina kupititsa patsogolo ndi kulimbikitsa chitetezo; komanso nthawi zina kupondereza achinyamata ndikuwalepheretsa pamoyo wawo,”¹⁰ taika mtima pantchito yathu yozamitsa ndi kulimbikitsa zochita zathu pothana ndi mavuto a SRHR. Kutsatira maphunzitso a zikhulupiriro zathu tikupita patsogolo kulimbikitsa umoyo wabwino wa anthu athu onse.



Mfundo zalembedwa pano zikuyimira malingaliro aakatswiri azauzimu ochokera magulu osiyanasiyana azachipembedzo, pokhudzana ndi mavuto a nkhani ya SRHR kumwera kwa Africa. Chinanso, ndikunenapo zakufunikira kwa chipembedzo pazokambirana ndi zochita zokhudzana ndi SRHR m'magulu osiyanasiyana.

2. ZOMVETSA ZATHU ZAKUFUNIKA KWA ZOGONANA, UMOYO WAUCHEMBERE NDI UFULU

Ngati magulu achikhulupiriro, tikupemphedwa kuti tisamalire “munthu wathunthu,” ndiye kuti, kumuganizira munthu pazonse. Tayanjanitsidwa ndi miyambo yazipembedzo zathu zosiyana kuti tigwire ntchito yokhudzana ndi ubwino wa thupi, chikhalidwe, uzimu, m'maganizo, nzeru, ndale, chitetezo, chuma ndiponso chilengedwe. Choncho, nkhani zokhudzana ndi umoyo wakugonana ndi uchembere ndi ndizofunikira pazenizeni zamagulu achipembedzo. Tikudziwa bwino zovuta zambiri zaSRHR zomwe achinyamata mdera lathu amakumana nazo.

"Tikubweretsa nnkhope yachifundo ya Mulungu pazokambirana za ufulu ndi umoyo wa zogonana ndi uchembere"

Father Oliver Siandele

Makamaka takhumudwa ndi kuchuluka kwa mimba za atsikana, nkhanza zochitika pakati pa amuna ndi akazi komanso kufala kwa kachilombo ka HIV pakati pa atsikana m'derali.¹¹ Taonanso kuti paintaneti m'madera mwathu mukuchitika nkhanza zosiyanasiyana, makamaka pakati pa ana ndi paachinyamata.

Timakumana ndi kukambirana pafupipafupi ndi anthu, mabanja am'madera ndipo ndife oyenera kulimbikitsa umoyo pazonse. Timalangiza anthu "kuyambira kuchiberekero mpaka kumanda" ndipo ndife ofunika kopambana kkuti ntchito za SRHR ziyende bwino m'madera, mdziko lonse komanso mzigawo. Kuchokera mzipembedzo zathu zosiyanasiyana, timamvetsa kuti SRHR ndi:

Chikhulupiroro chathu chimalimbikitsa anthu onse, kuphatikiza ana ndi achinyamata, kuti apeze nzeru zopatsa moyo. Kupeza zidziwitso zoyenera msinkhu, zolondola komanso zamakono za m'mene matupi athu amagwirira ntchito, kulimbikitsa umoyo wogonana ndi

Ufulu wa anthu onse kupeza nzeru, zidziwitso ndi ntchito zokhudzana ndi umoyo wawo, ntchito zogonana ndi uchembere moteteza umunthu ndi ulemu kwa onse. Umoyo ndi ufulu wazogonana ndi uchembere umasonyeza zofuna za anthu onsekuti akhale m'mene alawalengera ndikupatsidwa ulemu ngati anthu¹².

kupewa zandewu, zimapatsa anthu mpata wabwino wothandiza nawo pachitukuko chamdziko ndi m'madera. Tikulimbikitsa anthu athu kuti asake nzeru zokhudzana ndi SRHR kuti, pomodzi ndi maphunziro a zipembedzo zathu, asankhe zinthu mozindikira. Kusaka nzeru ndiye chimake cha maphunziro a zipembedzo zathu, ngati m'mene zalongosoledwe pansipa.

Polimbikitsa ntchito zaphindu za SRHR, anthu athu achipembezo kumwera kwa Africa adzakhala



akuthandizapo pazolinga zachitukuko zapadziko lapansi zodziwika kuti SDG. Zolingazi zikugwirizana ndi chikhulupiroro chathu. Mwachitsanzo, kuyika mtima pa SRHR kudzathandiza kuti tikwaniritse mfundo SDG 3, yomwe ndi "Kuonetsetsa kuti pali moyo wathanzi kwa anthu onse ndikulimbikitsa moyo waubwino kwa anthu amibadwa yonse," ndi mfundo SDG 5, yoti "Kukwaniritsa kufanana pakati pa akazi and amuna ndi kulimbikitsa amayi ndi atsikana."

Zolembe zathu zopatulika ndi maphunziro, miyambo ndi ziganizo zikutitsogolera popereka yankho ku SRHR. Zina mwazinthu zofunikira zafotokozedwa munsimu.

2.1. Kulengedwa mofanana

"Kwa Mulungu, tonse tili ndi nkhope imodzi"

Imam Lawrence Tsuro

Tkukhulupirira ndipo tikugwiritsa mfundo yoti amuna ndi akazi analengedwa ofanana. Tikuvomereza kuti nthawi zina chiphunzitso, matanthauzidwe amalembe opatulika ndi machitidwe athu sanawonetsa zoonazi. Nthawi zambiri, tagwiritsapo vuto lotanthauzira malemba athu opatulika kuti tilole anyamata ndi abambo kuti adzikhala ndi mwayi woposa atsikana ndi amayi. Zotsatira zazimenezi zakhala zomvetsa chisoni, m'magulu athu azipembedzo komanso m'magulu ena. Kupondereza atsikana ndi amayi kwaimitsa chitukuko cha mabanja athu, midzi, mayiko ndi madera.

Chipembedzo cha Bahai

"Dziko laumunthu tili ndi mapiko awiri - limodzi ndi akazi ndipo amuna linalo. Mpaka pomwe mapiko onsewo atakula bwino ndi pamene mbalamoyo imatha kuuluka. Ngati phiko limodzi likhalebe lofooka, kuuluka ndikosatheka. Mpaka pomwe dziko la akazi lidzakhale lofanana ndi dziko la amuna pakupeza zabwino ndi zangwiro, ndi pamene kupambana kungapezeke momwe zimayenera kukhalira." **Zosankhidwa mu Zolembe za 'Abdu'l-Baha, gawo. 227 p. 302.**

Chikhristu

"Palibe Muyuda kapena wakunja, kapolo kapena mfulu, palibe mwamuna kapena mkazi, chifukwa nonsenu ndi m'modzi mwa Yesu Khristu." **Galatiya 3:28**

Chisilamu

"Ndipo wokhulupirira, amuna ndi akazi, ndi abwenzi wina ndi mnzake. Amalalikira za ubwino ndipo amaletsa zoipa. Amatsatira salat, amalipira zakat ndipo amamvera Allaf ndi Mtumiki Wake. Ndi pazimenezi pamene Mulungu adzawachitire chifundo" **Quran 9:71**

Tikufuna kulimbikitsa katanthauzidwe kabwino kamalemba opatulika kuti awonetse ulemu wa anthu onse. Madera athu achipembedzo adzapitilizabe kuyesetsa kuphunzitsa ndi kulongosola mfundo yakuti anthu onse, kaya ndi amuna kapena akazi, amalengedwa ofanana.

Kutengapo mbali kwathu mu SRHR ngati magulu azipembedzo kumwera kwa Africa, choncho, kumalimbikitsidwa ndi mfundo iyi:

- Kuonetisa nkhope ya Mulungu**

Timawona anthu ngati "opangidwa modabwitsa" (Masalmo 139: 14) ndi "onse olengedwa ndi Mulungu" (Quran 39: 6). Magulu athu achipembedzo amaika mtima mu SRHR chifukwa imathandiza anthu kukhala ndi moyo wosangalala ndiponso wokwaniritsidwa. Munthu aliyense ndiwofunika ndipo amayenera kulemekezedwa chifukwa iye amawonetse chithunzi cha Mulungu. Anthu amakhala ndi ulemu wachibadwidwe. Choncho, njira yathu ku SRHR ndiyosasankha, popeza tikufuna kuwonetsetsa kuti anthu onse apeze zidziwitso ndi ntchito zabwino molangizidwa ndi miyambo ya zipembedzo zathu.

- Kusama mwachifundo**

Zipembedzo zathu zosiyana zimanena poyera: tili ndi udindo woyang'anira wina ndi mnzake. Ndife osamalira abale ndi alongo athu. Ngati anthu, sindife tinthu tomwe timangoyandama mosagwirizana. Mwambo wathu uliwonse umatiphunzitsa kuti tili ndi udindo wosamalirana. Kudera lakumwera kwa Africa, chiganizo cha Ubuntu, "Ndili chifukwa uli, ndipo chifukwa tili, ndiye kuti ndili," chimalimbikitsa mgwirizano. Ndiye choncho, kunena kumbali ya chipembedzo chathu, timayima mwamgwirizano ndi ana ndi achinyamata komanso ndi achikulire, akamakambirana nkhanu za SRHR. m'moyo. Choncho tili ndi udindo wopereka chithandizo kwa atsikana

omwe amatenga mimba, abambo achichepere, komanso achinyamata omwe anakumanako ndi nkhanu zapakati pa amuna ndi akazi.

- Ulemu kwa onse**

Kunyozedwa ndi kusolidwa ndi anzathu sizigwirizana ndi maziko achipembedzo chathu. Ngati anthu achipembedzo, tikutsimikizira kufunikira kwa ulemu wa anthu onse. Sitifuna kuyanana ndi omwe amadzudzula, kunyoza ndi kusala ena m'dzina la chipembedzo chathu. Timalimbikitsa chikhulupiriro chanthu anthu onse amayenera kulemekezedwa ndipo kuti ulemu wawo usapeputsidwe. Ulemu waumunthu ndiwofunikira paziganizo zanthu za SRHR m'mabanja mwathu, mdera lathu, mayiko athu ndi malo ena. Muchikhristu Genesis 1: 27 amafotokza kuti munthu adalengedwa m'chifanizo cha Mulungu. M'chisilamu ulemu waumunthu (karamah) ndizomwe zili m'ndime ya Koran kuti: "Tawapatsa ulemu ana a Adamu ndikukhazikitsa pa iwo zabwino zapadera zachilengedwe chathu." (17:70). Muchipembedzo cha Bahai, kufanana ndiponso ulemu waumunthu zimawoneka ngati chimodzimodzi pakati pa amayi ndi abambo: "Akazi ali ndi ufulu wofanana ndi amuna padziko lapansi; muchipembedzo ndi m'magulu iwo ndiwofunikira kwambiri. Nthawi zonse pamene amayi akuletsedwa kukwaniritsa zomwe angathe kuchita, amunanso azilephera kukwaniritsa zazikulu zomwe amayenera kukhala nazo." (Abdu'l-Baha: "Kulimbikitsidwa kwa Mtendere Wonse")



- Nthumanzi**

Pamodzi ndi zolembe zathu zopatulika, ziphunzitsa ndi miyambo, chikumbumtima cha munthu aliyense chimathandiza kwambiri pazokhudzana ndi SRHR. Zipembedzo zathu zosiyana amagwirizana pokhulupirira kuti Mulungu anadalitsa anthu ndi chikumbumtima. Ili ndiye "liwu lamkati" lomwe limathandiza anthu azipembedzo zosiyanasiyana kusiyanitsa chabwino ndi choipa. Chikumbumtima ndi chida champhamvu chomwe chimathandiza anthu achipembedzo kupeza mayankho pazokambilana za SRHR, pamodzi ndi zolembe zopatulika ndi ziphunzitsa zopezeka mzikhalidwe zathu.

2.2. Udindo wa chipembedzo pakulimbikitsa chilungamo kwa onse

"Kusowa chilungamo kwa m'modzi ndikusowa chilungamo kwa tonsefe ngati gulu lachipembedzo. Tiyenera kubwerera kwa anthu amene tatumidwa kuti titumikire osati kulamilira."

Bishop A.M.Mnisi

Mfundo ina yomwe imatitsogolera popeza mayankho a SRHR ndikuti chipembedzo chenicheni chimalimbikitsa chilungamo kwa onse. Chipembedzo sichili pachokha kapena kutali ndi zochitika mdziko. Ndiponso, Chipembedzo chathu chimayenera kukhazikitsidwa ndikufotokozedwa munjira zomveka. Kafotokozedwe kachipembedzo chathu kamakhazikitsidwa pa mfundo iyi: Osavulaza.

Chipembedzo chathu ndi zifuniro zathu zimatsogolera okhulupirira. Timfuna kusamalira anthu achikhulupiriro kuti akhale okonzeka kuthana ndi mavuto omwe akukumana nawo. Timatsogoleredwa ndi mfundo zachikondi, kuvomerezedwa, chifundo ndi umodzi. Chifukwa chake, timayesetsa kuperekezana paulendo ndi achikhulupiriro. Timafuna "kumvetsera mwachikondi," makamaka povomereza kuti ana ndi achinyamata akhoza kulakwitsa. Komabe, timaona kuti ndiudindo wathu kukhalapo ndi kuthandiza anthu ndi mabanja pamoyo wawo, wokhala ndi zosangalatsa ndi zovuta.

2.3. Falitsani uthenga: Kugwiritsa ntchito mabwalo tili mwao kale konkuno komonso akwina

"Yendani nafe njira iyi yachikhulupiriro. Maphunzitso achiBahi amati kuphunzira ndikofunika kwambiri. Ngati sindignaphunzitse mwana wanga ndiudindo wanga kuphunzitsa mwana wamdera langa."

Abdia Naidoo

Ife tajjirika kale kufuna kupeza mayankho azinthu za SRHR m'magulu osiyanasiyana, ngakhale tikuvomereza kuti bwenzi tikuchitapo zambiri. Mwachitsanzo, ena mwa magulu athu azipembedzo apanga mfundo ndi malangizo okhudzana ndi maphunziro azazimu kuti athane ndi zovuta za SRHR. Ena akuyendetsa ntchito zothana ndi


nkhanza za pakati pa akazi ndi amuna, monga "Lachinayi Lakuda". Ntchito zina ndi misonkhano yokambirana ndi ana komonso achinyamata, kusinkhasinkha zamalemba opatulika ndi SRHR, kuchotsa miyambo ndi zikhalidwe zopondereza akazi kulowetsapo zikhalidwe zopereka ufulu ndi zina. Timayendetsa sukulu ndi malo azaumoyo omwe amapereka chithandizo cha SRHR ndi zidziwitso zokhudzana ndi chipembedzo chathu. Ngati chikhulupiriro chathu sichilola, timatumiza makasitomala athu kumabungwe ena omwe angachite bwino kuposa ife. Komabe, tikudzipereka kuchita ntchito zotsatirazi kuti tiwonjezere zoyankha zathu zokhudzana ndi SRHR.

- **Kulalikira kuchokera malo opatulika**

Ndikofunikira kwambiri kuti tigwiritse ntchito malo opatulika omwe tili nawo, kufalitsa uthenga wabwino wa SRHR. Tili ndi mwayi wapadera wokhala ndi omvera ambiri omwe amasonkhana kupemphera ndikusinkhasinkha pamasiku osiyanasiyana asabata. Tidzayesetsa kukulitsa mwayi womwe tili nawo wofalitsa mauthenga opatsa moyo pazokhudzana ndi SRHR kuchokera kumabwalo opatulika omwe tili nawo m'madera athu. Tikufuna pakhale malangizo aulaliki kuti kutanthauzidwe ka malemba opatulika kafanane ndi kutinso tithetse kutanthauzira kolakwika.

- **Wailesi ya dera**

M'malo ambiri, magulu athu azipembedzo amakhala ndi



nyumba zowulutsira mawu pawayilesi. Tichitapo zambiri kuwonetsetsa kuti tikugwiritsa ntchito nyumba zowulutsira mawu pawayilesi fufalitsa zidziwitso zoyenera za SRHR. Nyumbazi ndizofunikira kwambiri kuti tigawane maganizo, zidziwitso ndi machitidwe abwino okhudzana ndi SRHR m'madera athu. Zimapereka chidziwitso kwa anthu ovuta kufikira omwenso timawatumikira, kuonjezapo nkhanu zaubwenzi, chuma, chikhalidwe, maphunziro, umoyo, madzi ndi ukhondo komonso tsoka ndi zina.

- **Kulemba**

Ngakhale kuti anthu athu achipembedzo akugwira ntchito zina zokhudzana ndi SRHR, nthawi zambiri zimenezi zimakhala zopanda zikalata. Chimodzi mwazovuta zathu m'magulu azachipembedzo ndichakuti timachita zinthu zambiri, koma sitizilemba. Chifukwa cha ichi, tikufuna

CHIPEMBEDZO CHA BAHAI CHITHANA NDI VUTO LANKHANZA NDI KUGONANA PACHIBALE PABANJA

Zaka zingapo zapitazo, zinachitika ndizoti banja lina linakalowa m'chipembedzo cha Bahai. Pasanapite nthawi yaitali kuchokera pamene analowa mumpingowo, mmodzi mwa atsikana awo anatenga mimba. Zachisoni ndi zoti panthawiyo atsikana ambiri mdera limene banja limakhalalo amapezeka ndi vuto lomwelo. Mimbayo itadziwika mtsikanayo anayamba kumajomba kuzinthu zonse zauzimu zam'mudzi ndipo mwana atabadwa, anayamba kuamapita kumisonkhano ina mwakachetechete. Komabe, bungwe lauzimu lidazindikira zakulakwa kwakukulu komwe msungwanayo

anachita ndipo atakambirana ndi

banjali lidatsimikiza kuti bambo adagwiririra mwana wawo wamkaziyo. Kuululaku kunali kodabwitsa ndipo bungweli linayenera kupeza njira yothanirana ndi nkhanayi imene inawononga moyo wa msungwanayo komanso banja lonse. Kudzera mnjira yokambirana ndi kufunsa akatswiri a chiBaha'i, banjali lidachitapo kanthu kukhaulitsa bamboyo, yemwe zimamvekanso kuti ankachitanso zachiwerewere ndi atsikana ndi amayi ena mderalo. Anaikidwa m'ndende.

Tsoka lake msungwanayo akuvutikabe m'maganizo chifukwa cha zokhumudwitsa zonsezi ndipo mwana wake wamwamuna nayenso akunzunzika ndi maganizo okhudzana ndi kubadwa kwake. Anthu ena

mbanjali anakhumudwa kwambiri mpaka anasamukira kuchigawo china kuthawa zamanyazi zimene zinachitika mnyumba mwawo.

Nkhani yowonayi ikungokhudza pang'ono zotsatira zankhanza yotereyi. Mtsikanayu ndi banja lake anali ndi mwayi wopeza chithandizo kuchokera ku magulu achipembedzo komanso mabungwe ake. Amayi ake anapitiliza kutumikira pantchito zachipembedzo mpaka anamwalira akugwirabe ntchito yachithandizo ndikuchiritsa anthu okhumudwa. Koma msungwanayo ndi mwana wake wamwamuna amasowabe kulandira chithandizo chauphungu ndipo masiku ena ampezako bwino koma ena ayi. Ichi mwina ndichimodzi mwazofunikira pamoyo wonse. Anthu achiBahai akupitilizabe kuthandiza banjalo.

tiyambe kulemba mwandondomeko ntchito zathu zonse za SRHR. Zimenezi ndizofunika tikafuna kuchita kawuni wantchito zathu. Zipembedzo zathu zimatilamula kuti tiwonetsetse kuti tikugwira ntchito moyenera komanso mokwanira, choncho kulemba, kuwunika ndi kuyesa sizinthu zachilendo kwa ife. Tidzayesetsa kupanga ndondomeko yopafupi yolembela malipoti yomwe idzagwirizane ndi njira zina zolembela malipoti.

- **Kambilanani ndi magulu azachipembedzo m'mabubgwe athu**

Tikuzindikira kuti mabungwe athu ali ndi magulu omwe amaonetsetsa kuti ntchito za SRHR zikugwirika moyenera. Ambiri mwamabungwe athu ndiwopangidwa malingana ndi msinkhu kapena kukhala akazi ndi amuna; mwachitsanzo, pali magulu a achinyamata, amayi, ndi abambo. Timayesetsa kugwiritsa ntchito maguluwa kwambiri kuti tilimbikitse kagwiritsidwe kabwino kantchito za SRHR.

- **Gwirizanani ndi okhudzidwa ena**

Limodzi mwamavuto omwe takumana nawo ngati magulu achipembedzo ndikuti nthawi zambiri timangodziyang'ana

tokha. Izi zimatilepheretsa kugwirizana ndi ena okhudzidwa omwe nawonso amafuna kupeza mayankho a SRHR. Anthuwa ndi monga akatswiri azaumoyo, aphunzitsi, andale,

Akatswiri a malamulo ndi ena. Nthawi zambiri, anthuwa ndi anzathu am'magulu azipembedzo zathu. Chonco, ndikofunika kuti tipeze mgwilizano ndi ena onse okhudzidwa ndi nkhanzi zaSRHR mdera lathu.

- **Gawanani ndi zipembedzo zina**

Tikuzindikira kufunikira kogwirizana ngati anthu achipembedzo. Ngakhale ena ayesetsa kulimbikitsa zigawo ndi mpikisano, ife tatsimikiza ndithu kuti tigwirire ntchito limodzi pothana ndi zovuta zokhudzana ndi SRHR zomwe timakumana nazo limodzi. Malembo athu opatulika amatsimikiza zakufunika kogwirira ntchito limodzi kuti zikomere onse. Tikukhulupirira kuti kugawana ndi anthu azipembedzo zina chuma chathu ndi zomwe takumana nazo, tidzakhala ndi ntchito za SRHR zothandiza kwambiri. Zimenezi zidzathandiza dera lathu kukhala lathanzi, lodzuka komanso lotikuka.

ZOWERENGA

1. Southern Africa Gender Protocol Alliance SRHR Policies and ... Figure 1: Number of countries with stand-alone SRHR policies & laws.
2. WHO Fact Sheet on Adolescent Pregnancy 2018.
3. Mapping HIV prevalence in sub-Saharan Africa between 2000 and 2017.
4. United Nations Children's Fund, Ending Child Marriage: Progress and prospects, UNICEF, New York, 2014, https://www.unicef.org/media/files/Child_Marriage_Report_7_17_LR..pdf
5. UNICEF https://data.unicef.org/wp-content/uploads/2015/11/UNICEF-Child-Marriage-Brochure-High-Single_246.pdf
6. UNICEF 'The state of the world's children 2015: Reimagine the future', data.unicef.org/wp-content/uploads/2015/12/sowc_2015_Summary_and_Tables_210.pdf
7. UNICEF https://data.unicef.org/wp-content/uploads/2015/11/UNICEF-Child-Marriage-Brochure-High-Single_246.pdf
8. *ibid*
9. For example, the Southern African Development Community (SADC) concedes that, "Gender based violence is known to be widespread in the Southern African Development Community (SADC) region and presents a major obstacle to attaining gender equality and equity." <https://www.sadc.int/issues/gender/gender-based-violence/>
10. UNFPA, "Enhancing Sexual and Reproductive Health and Well-Being of Young People: Building Common Ground between the United Nations and Faith-Based Development Partners," n.d., <https://www.unfpa.org/sites/default/files/pub-pdf/EnhancingSexualAndReproductiveHealth.pdf>
11. "Start Free Stay Free AIDS Free 2019 Report," UNAIDS, Geneva, 2019, p. 6. "The number of new HIV infections among adolescent girls and young women, many of whom become mothers, remains too high".
12. See G. Paterson and C. Long. 2016., eds., Dignity, Freedom, and Grace: Christian Perspectives on HIV, AIDS, and Human Rights. Geneva: World Council of Churches. This is a working, tentative definition of a faith-based approach to SRHR.

Mtsiriziro

Magulu azipembedzo ndiofunika kwambiri kuti ntchito za SRHR zikhale zopambana m'derali. Tili ndi anthu ambiri, mgwirizano wa akatswiri, chuma komanso kudzipereka kuti tipititse patsogolo ntchito zothandiza. Molimbikitsidwa ndi chipembedzo chathu komanso mtindi wa anthu odzipereka, tili ndi mlingo wopereka utsogoleri pazufina kupeza mayankho onse okhudzana ndi SRHR m'mabanja, m'madera, mdziko komanso kwina. Chipembedzo chathu ndi magari amoyo wathu. Chimapereka chitetezo ndi malangizo pantchito za SRHR zomwe timachita. Chimalimbikitsa chidwi chathu ndikuwunikira paziganizo zozizwitsa. Chipembedzo chathu chimatsogolera m'mene tingatengere mbali pantchito za SRHR ndikutithandizanso kutsimikizira ena kuti chidwi cha ntchito zathu chikukhazikitsa maziko olimba othandiza kuti ntchitozo ziyende bwino m'chigawo chonsechi.

MALANGIZOWA ANAKONZEDWA NDI MABUNGWE AWA:



ACT UBUMBANO



The Methodist Church of Southern Africa
A Christ healed Africa for the healing of nations

actalliance

